

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso  
kuchokera m'Baibulo kupita kwa  
amene akulalikira Uthenga Wabwino

## MDIEREKEZI, ALI MONGA MKANGO WOBUMA

*Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu  
mdierekezi, monga mkango wobuma,  
ayendayenda ndi kufunafuna wina  
akamlikwire. amenyo mumkanize okhazikika  
m'chikhulupiriro.... —1 Petro 5:8*

Mu chaka cha 1898, panali ntchito yomanga njanje ya sitima ya patmtunda kuchokera ku Kenya kupita ku Uganda. Njirayi imadutsa m'malo amene anali ndi zigwembe zochuluka. Panali unyinji wa anthu amene amagwira nawo ntchitoyi ndipo panali malo ambiri osungirako zida zogwirira ntchito. Posakhalitsa anthu ogwira ntchito anayamba kusowa ndipo ena anadziwa kuti panali mikango iwiri yolusa imene inali kugwira ndi kudya anthu m'deralo. Mikangoyi inavutitsa kwambiri kwa miyezi yokwana 9, ndipo inapha anthu ambiri ndipo izi zinadzetsa mantha kwa anthu ogwira ntchito ochuluka. Mikangoyi imafika pa malo osiyanasiyana m'mbali mwa njanjeyo ndipo imapha ndi kupweteka anthu ogwira ntchito aja. Iwo anayesa kuika misampha kuti mikangoyo ikodwe koma izi sizinathandize. Ogwira ntchito aja anapanga mpanda wozungulira wokhala ndi minga ndipo amayatsa moto pofuna kupirikitsa mikangoyo, koma iyo imadumpha mpandawo kapena kukwawa pansi pake. Ikatero imagwira anthuwo kuchoka mu ma tenti amene anthuwo amagona kenaka ndi kuwakokera kuthengo. Anthu otsalawo amaimva mikangoyo ikuwapwetedza anthu ogwidwawo komanso ikubuma kusonyeza kuti yakhuta. Tangoganizani mantha amene anthuwo amakhala nawo pamene akuyenda mu mdima, makamaka pozindikira kuti mikango yodya anthuyo ili pathengo chapafupi pompa.

Mikangoyo imamveka ikubuma chapafupi ndipo anthu oyandikira amatumizirana uthenga namati: "Samalani abale, Mdierekezi uja akubwera!" Mantha amagwira anthu onse

pamalopo ndipo zoonadi pofika m'mawa kumapezeka kuti m'modzi mwa ogwira ntchito aja wasowapo. Patapita nthawi ndipo miyoyo yambiri itatayika, pamapeto pake mikangoyo inaphedwa.

Mtumwi Petro akutichenjeza kuti tikhale maso ndi odzisungira pozindikira kuti Mdierekezi ali ngati mkango wobuma. Mdierekeziyo, monga ngati mikango iwiri ija, akufuna kubweretsa mantha m'miyoyo ya Akhristu ndipo akuchita zonse zimene angakwanitse kuti aphe, abe ndiponso aononge miyoyo yathu yauzimu. Nkofunikira kuti tikhale maso ndi odikira kuti tionetsetse magawo amene mdierekezi akugwira ntchito. Iye akufuna kutibera chimwemwe chathu, mtendere wathu ndi umodzi wathu. Iye akufuna kuti inuyo musiyanitsidwe ndi anthu a Mulungu, ndipo mukhale kutali ndi iwo amene akhoza kukulimbikitsani ndi kukuthandizani.

Mdaniyo akumenya nkondo kuchokera m'malo osiyanasiyana ndipo akulimbana kwambiri ndi oyera mtima. Iye salemekiza munthu. Ngati muli ake a Mulungu, iye amafunitsitsa kuti akugonjetseni—nakupwetekeni mu nkondo iyi yauzimu. Mdaniyo akulimbana ndi anthu m'miyoyo yawo, iye akuponya mivi yake pa mabanja ndi mipingo. Tiyenitsekule maso athu ndi kumuzindikira mdani weniweni. Ino si nthawi yogona kapena kuthawa nkondo yake. Mukanizeni iye molimba mtima ndi mwachikhulupiriro!

Yesu anauza ophunzira ake kuti "Chezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa: mzimutu uli wakufuna, koma thupi lili lolefuka." (Mateyu 26:41). Tikadali m'thupi ndipo tikhoza kugonja m'mayesero pamene tikukhala padzikolo lino lapansi. Sitinafike kumwamba, choncho tikuyenera kukhala maso ndi opemphera kuopa kuti tingataye



"Mdierekeziyo...  
akufuna kubweretsa  
mantha m'miyoyo  
ya Akhristu  
ndipo akuchita  
zonse zimene  
angakwanitse kuti  
aphe, abe ndiponso  
aononge miyoyo  
yathu yauzimu."

# ZIMENE BAIBULO

## LIMAPHUNZITSA ZA...

### Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

### Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

### Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

### Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;  
Aef. 2:1, 5-6

### Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

### Chidzalo cha Mzimu Woyeria

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

### Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;  
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

### Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

### Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;  
Akor. 1:18

### Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

### Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;  
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

### Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

### Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;  
1 Akor. 7:10-11

### Chikhaliidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

### Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;  
Mat. 25:31-46

### Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

### Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

### Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

njirayo ndipo nkubwerera kudziko. Pemphero ndicho chida chimodzi chimene chikhoza kutithandiza kuti tigonjetse nkhondo zonse zochokera kwa mdaniyo. Thupili lili lofooka zedi ndipo kungofuna Mulungu pakokha sikuli kokwanira kuti titetezedwe ku mphamvu ya mdaniyo. Tikuyenera kukhala tcheru ndipo tisaleke kufunafuna chisomo ndi mphamvu zochokera kwa Mulungu.



**“Satana anafunsa akutengeni kuti akupeteni ngati tirigu; koma ndinakupempherera kuti chikhulupiriro chako chingazime; ndipo iwe, pamene watembenuka ukhazikitse abale ako.”** Ndi zoona ndithu kuti kufikira lero Satana amafuna kukutengani INUYO. Yesu akukupemphererani ndi kukupembedzerani inuyo pamene Iye ali padzanja lamanila Mulungu. Nkhani yabwino ndio yakuti mphamvu ya Mulungu ndi yoposa kutilitali mphamvu ya mdierekezi. “Inu ndinu ochokera mwa Mulungu, tiana, ndipo munailaka; pakuti Iye wakukhala mwa inu aposa iye wakukhala m'dziko lapansi. Iwo

ndiwo ochokera m'dziko lapansi” (1 Yohane 4:4). Ngati mukhala ndi Mulungu tsiku ndi tsiku, Iye adzakutetezani ndi kukuyang'anirani ndipo adzakuikirani njira yakuti mugonjetse mphamvu ya mdierekezi, koma mukuyenerabe kukhala tcheru ndi osamala mu zisankho zosiyansiyana za moyo wanu. Khalani anzeru ndipo musalolele kuti mupezeke pamalo pamene mukhoza kuvulazidwa. Khalani pafupi ndi Ambuye ndipo mukhale ndi chikhaliidwe chimene chidzakuthandizani kuti mulimbikitse ubale wanu ndi Mulungu. Kuunika kwa mau a Mulungu kudzawala pa mdaniyo ndi kuulula machenjerero ake onse. Mulungu adzapanga njira yakuti mupulumuke ku yesero lililonse ndipo adzapanga njira mu chigwa chilichonse komanso pa phiri lililonse limene mdaniyo angabweretse.

Pamene tikuyenera kusamala, nkofunika kuti tisachite mantha ndi mdaniyo pamene mphamvu ya Khristu ili pa ife. “Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iliyonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse.” (Luka 10:17-19). Mungathe ndipo mukhoza kugonjetsa machenjerero a mdaniyo pamene mukulimbika m'chikhulupiriro ndipo mukudalira mphamvu ya Yesu Khristu. Pamene nkondoyo ikupitirira, tikuyenera kulimbika kumukaniza mdierekezi mwachikhulupiriro, ndipo tidzapeza chitetezo chachikulu mu chisomo cha Yesu Khristu chimene chimapulumutsa. Izi ndi zokwanira kuti zititengere tonsefe kuti tikafike bwino kwathu Kumwamba. ■

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandre ngati mukufuna kuti mudzialidira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwalere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalam zimene ena amapereka mwafulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.org

# Mau a Mkonzi



*Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulanso mwini wake kuntchito zake, monganso Mulungu kuzake za Iye. Chifukwa chake tichite changu cha kulowa mpumulowo, kuti wina angagwe m'chitsanzo chomwe cha kusamvera. —Ahebri 4:9-11*

Mutu wathu ulendo uno ukakamba za nkhani yokhudza chitetezo chamuyaya kapena kuti "munthu ukangopulumuka, basi wapulumuka mpaka muyaya."

Chipunxitso cha chitetezo chamuyaya ndi imodzi mwa mfundo zazikulu za chipunxitso cha munthu wina dzina lake John Calvin ndipo chimatchedwa kuti Calvinism. Mfundu imene ili yotsutsana nayo kwambiri ndiyo ya Arminianism imene inayamba ndi munthu wina wotchedwa Jacob Arminius. Ziphunxitso ziwiri izi za mau a Mulungu zinagawanika pa mfundo ya kuti Mulungu ndiye wopanga zonse, munthu ndi wochimwa, kupangiratu, kuchita chopepesera kwa Khristu, chisomo, chifuniro cha munthu, ndi kusungika. Mitu imeneyi ndi yolukanalukana popeza umodzi umakhudzana ndi unzake. M'malo mwakuti indinene tsatanetsatane wa zimene Malemba akunena pa mutu uliwense, chifukwa chakuti maloakanakwanira, ndangoganiza kuti ndingokamba mwachindunji koma mwachidule zimene Malembawo akunena. Pamene ndikukhulupirira kuti chi Arminianism ndicho cholondola kusiyana ndi chi Calvinism, malemba ndiye amene akhale chotitsogolera, osati chipunxitso cha munthu ayi. Kawirikawiri pamakhala mfundo zina zing'onozing'ono zimene zili zoona ku mbali zonse ndipo zikhoza kuyiwalidwa chifukwa chakuti munthu ukufuna kusyanitsa pakati pa mfundo ziwirizi.

Mfundu yakuti "munthu ukangopulumuka, basi wapulumuka mpaka muyaya" ndi chachidziwikire siyochokera kwa Mulungu ndipo ikhoza kuwapatsa anthu chiyembekezo chabodza kuti iwo ali otetezedwa. Ndi chipunxitso choopsa chimene chimatsekula khomo lakuti tilolele uchimo pa moyo wathu pogwirtsia ntchito chisomo ngati chinthu chophimbira zoipa zimene tikufuna kuchita. Ngakhale kuti chipunxitsochi si cha mu Baibulo, pali malemba ambiri amene anthu otsatira John Calvin amawagwiritsa ntchito amene ali ofunikira kuti timvetsetse bwino zina zokhudza cholinga cha Mulungu pa ife anthu. Mulungu waitana ana ake kuti akhale ndi moyo wachiyero ndipo wosachimwira dala popeza uchimo umasiyanitsa munthu ndi Mulungu. Nzotheka kuti tikhaza kukula mwa Ambuye ndiponso kuti tifikitse chiyero chathu. Ngati sitikusamala, Mpingo wa Mulungu ukhoza kuhazikika kwambiri pa zintchito ndipo anthu akhoza kuyamba kudalira ndi kuika chikhulupiro chawo mwa ntchitoto. Pamene ntchito zili chionetsero cha chipulumutso chenicheni, ntchito sizingatipulumutse ndipo sizingatipangitse kuti tikhale wopulumuka. Timapulumuka mwa chisomo cha Mulungu ndiponso kudzera mu mwazi wa Yesu wochita chopepesera. Palitu chitetezo chimene chimachokera ku kudziwa kuti Mulungu amafunitsitsa kukhululukira ndi kubwezeretsa osati kutaya. Kudziyenereza nthawi zambiri kumachitika chifukwa chakuti anthu akhazikika kwambiri pa mfundo ya ntchito.

Chipulumutso ndi ntchito ya Mulungu imene imatimasula ku mphamu ya uchimo. Aphunzitsi a chitetezo chamuyaya amatsindika mfundo yakuti iwo amene sakhalupirira mu chipunxitsochi amachepepta mphamu ya mwazi ndi chisomo cha Mulungu. Ndikukhulupirira kuti nkolondola kwambiri kutero kusiyana ndi kutembenuza zinthu. Kumakhala ngati sitikuvomera kapena kukhulupirira kuti mwazi wa Yesu komanso chisomo cha Mulungu zilibe mphamu yokwanira yakutiteteza kuti tisabwererenso ku uchimo. Mphamu yaikuluyo ndiyo imene imateteza, ndikusunga. Imeneyi ndiyo mphamu ya mwazi ndi chisomo. Imasiyana ndi kuditiriza kuchita chopepesera nsembe ya uchimo. Ntchito yathu ndiko kulimbikitsa chikhulupiro posunga mphamu ya Mulungu ndi kumvera Mau ake mwa kuthekera kwa chisomo chake.

Malemba akunena momveka bwino kuti munthu akhoza kutaya chikhulupiro chake ndi moyo wosatha ngati sasunga chiyanjano chake ndi Mulungu. Choncho, chipunxitso cha chitetezo chamuyaya chili cholakwika, koma ife nafenzo sitikondweretsedwa ndi chipunxitso chabodza chakuti chipulumutso sichikhala chamuyaya. Kukoma kwa chipulumutso chenicheni ndiko kwakuti pali mpumulo umene umachokera kwa anthu a Mulungu pamene tasiya kudalira ntchito zathu. Ndikuthokoza kuti ndine wotetezeza kwamuyaya mwa chisomo ndi chikondi cha Mulungu. Tikhale okhulupirika ndi kusankha kuti chitetezo chimenecho koposa zinthu za dziko lino.

Michael W. Smith

April 2019

Zambiri Zili pa  
**INTANETI**

**Mukafuna kutipeza**


**pa intaneti, mulembe**

**[www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org)**

**kuti mudzilandira makalata**

**athu kabenango kuti**

**muone makalata akale.**



# Kalozera posanthula Baibulo

## Mutu: Chiterezo chamuyaya

**Kuwerenga Mau a Mulungu:** Koma wolungama wangayo adzakhala ndi moyo wochokera m'chikhulupiriro: Ndipo ngati abwerera, moyo wanga ulibe kukondwera mwa iye. Koma ife si ndife a iwo akubwerera kulowa chitayiko; koma a iwo a chikhulupiriro cha ku chipulumutso cha moyo. —Ahebri 10:38-39

**Tanthauzo:** Chiterezo chamuyaya [kapena kunenango kuti "masungidwe a oyera mtima" malingana ndi m'mene amaphunzitsira John Calvin, kapenango kunena kuti "munthu ukangopulumuka, basi wapulumuka mpaka muyaya"] ndi mau amene amawatanthauzira mosiyanyasiyana. Koma nkhani yake ndiyo yakuti, chimenechi ndi chiphunzitsi chomwe chimatsindika kuti pamene munthu watembenuka mtima kapena wabawda mwatsopano, palibenso chimene angachite kuti asinthe maonekedwe ake. Chiphunzitsi ichi chimanena kuti pamene munthu wavomerezaa Khristu ndi kupulumuka, Mulungu adzamusunga munthuyo kuti asachimwenso ndipo chipulumutso chake chili chotetezeza kwamuyaya ndipo palibenso chingachitike kuti iye ataye chipulumutsocho.

**Kunena mwachidule:** Chipulumutso cha munthu chimachitika mwa chisomo cha Mulungu basi ndipo sichochokera ku ntchito. Mulungu mwa chisomo chake adzakhala okhulupirika kusunga munthuyo kuti athe kukhala m'moyo wachiyero. Chipulumutso ndi ubale wa pangano la chikhulupiriro, kuti ngati munthuyo asankha kupatuka kuchokera ku chikhulupirirocho ndi kudzipereka kwa Mulungu, ubalewo umatha ndipo chipulumutsocho chimatayika. Ngakhale kuti chipunzitsi cha chiterezo chamuyaya kapena mau akuti "munthu ukangopulumuka, basi wapulumuka mpaka muyaya" akhoza kupumula mwa chisomo chimene chimapezeka pakukhulupirira Khristu.

### I. Chipulumutso chimachokera ku chisomo mwa chikhulupiriro

- A. Aefeso 2:8-9 Ndinu opulumutsidwa mwa chisomo (Aroma 5:1).
- B. Ahebri 7:25 Mulungu apulumutsa akutali kwambiri.
- C. 2 Akorinto 5:17 Cholengedwa chatsopano mwa Khristu.

### II. Moyo wosatha uli mphatso ya Mulungu

- A. Yohane 5:24 Iye amene akhululupirira ali nawo moyo wosatha (1 Yohane 5:11-13).
- B. Yohane 6:37-40 Kwa iye wakudza, Yesu sadzamupirikitsa.
- C. Aroma 6:20-23 Mphotho ya uchimo ndiponso mphatso ya Mulungu.

### III. Chiterezo mwa Mulungu

- A. Yohane 10:27-29 Nkhosa za Khristu sizidzatha.
- B. Aroma 8:35-39 Palibe chimene chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu.

### IV. Mulungu ali wokhulupirika kuti asunge

- A. Yuda 1:24 Amakutetezani kuti mungagwe (1 Petro 1:5).
- B. 2 Akorinto 1:22 Mulungu amasindikiza wokhulupirirayo (Aefeso 4:30).
- C. 1 Akorinto 1:8-9 Kutsimikizika mpaka kumapeto.
- D. Afilipi 1:6 Mulungu adzamaliza ntchitoyo.

### V. Kufotokoza za ubale wa uzimu

Yohane 15:1-11 Wokhulupirira akhalebe mwa Khristu, mpesawo.

### VI. Chiyero ndi chofunikira

- A. 1 Akorinto 6:9-11 Anthu osalungama sadzaulaŵa Ufumu wa Mulungu.

- B. Ahebri 12:14-15 Tsatani chiyero kuopa kuti mungadetsedwe.

- C. 1 Yohane 1:6 Kunena kuti timayanjana naye tili mu mdima ndi bodza.

### VII. Chitsimikizo chakuti chipulumutso chikhoza kutayika

- A. Mateyu 13:3-9 Fanizo la wofesa mbeu.
- B. 1 Timoteo 4:1 Anthu ena adzataya chikhulupiriro chao (Machitidwe 20:28-30).
- C. Agalatiya 5:1, 4 Mudalekana ndi madalitso aulere a Mulungu.
- D. 1 Timoteo 6:9-11 Adasiya njira ya chikhulupiriro.
- E. Ahebri 3:12-14 Kusakhulupirira kumamlekanitsa ndi Mulungu.
- F. 2 Yohane 1:8-9 Musataye zimene mwagwirira ntchito.
- G. Chivumbulutso 3:3-6 Zovala zodetsedwa.
- H. 2 Petro 2:20-22 Ogidwa ndi kugonjetsedwa.
- I. 1 Akorinto 3:16-17 Mulungu adzaononga kachisi wodetsedwa.

**Onaniso:** 1 Akorinto 9:27, 2 Petro 3:17, Aroma 11:21-23, 2 Timoteo 2:17-19.

### VIII. Kulimbikitsidwa kuti tikhale okhulupirika

- A. Akolose 1:21-23 Osasunthika pa chiyembekezo.
- B. 1 Akorinto 15:58 Limbikani, khalani osagwedezeza.
- C. Ahebri 4:14 Tigwiritse chikhulupiriro chimene timavomereza (Ahebri 3:14).
- D. 1 Timoteo 6:12 Mukalandire moyo wosatha.

### Kumaliza

Khala wokhulupirika kufikira imfa, ndipo ndidzakupatsa iwe korona wa moyo. —Chivumbulutso 2:10b

# CHITETEZO CHAMUYAYA



## Dongosolo la chipulumutso

Mafunso okhudza chitetezo chamuyaya alipo ambiri ndipo mayankho ake amakhudza unyinji wa zinthu zaumulungu. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa akatswiri a Baibulo ndipo pali malemba amene aliyense

wa iwo amagwiritsa ntchito pofuna kuchitira umboni mbali yake, komatu malemba saphunzitsa ziphunzitso ziwiri zosiyana. Baibulo mu uthunthu wake limapereka dongosolo

labwino la ubale wa chipangano chachikhulupiriro chimene chilipo pakati pa Mulungu ndi munthu.

Mulungu adzaima pa Mau ake ndipo adzakhala wokhulupirika kwa ana ake, komabe pofuna kuti ubalewo ukhale wokwanira, ana akewo akuyenera kupitiriza mu chisankho chawo chotsatira Khristu ngakhale zivute motani. Wokhulupirira akuyenera kupitirira kukhala ndi mphamu ya kusankha kuti akhoza kukhala kunja kwa chikhulupiriro ndi kutsata moyo wa uchimo. Pakuchita izi, ndi chisankho chakecho, wokhulupirirayo ataya ntchito ndi cholowa cha chipulumutso.

## Chipunzitso chonyenga chimene chimaloleza kuti uchimo upitirire

Chipunzitso cha chitetezo chamuyaya chimakonda kudziwika kuti "ukapulumsidwa kamodzi, wapulumsidwa mpaka kalekale." Chipunzitso ichi chimatsekula khomo kuti uchimo upitirire pamene akunena zakuti ndi opulutsidwa ndipo amagwa mu dzenje la zinthu zaumulungu ponena kuti munthu amene wabwerera ku uchimo ndiye sanali wopulumsidwa. Mfundu zonse ziwigirizi sizikugwirizana ndi mau a Mulungu. Ngakhale kuti chipunzitso cha chitetezo chamuyaya chili chosalondola, pali mfundu zina zimene zili zoona mu chipunzitsochi. Tisamale kuti tisalekane ndi mfundu zoona chifukwa chakuti wina wake wazigwiritsa

Pali kusiyana kwakukulu pakati pa Akhristu zokhudza chipunzitso cha chitetezo chamuyaya. Pamene munthu wavomereza Khristu, kodi nkotheka kutaya chipulumutsocho kapena chipulumutso ndi choteteze ka kwamuyaya ngakhale munthu achite machimo?

ntchito ngati nsanamira pofuna kuumba chipunzitso chonyenga.

## Kupulumutsidwa mwa chisomo, osati ndi ntchito

"Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu" (Aefeso 2:8-9).

Chipulumutso sichochokera kuntchito koma ndi machitidwe akumwamba ndi mphatso ya chisomo cha Mulungu chimene chimabwera pamene munthu waika chikhulupiriro chake nadalira mwa Ambuye Yesu Khristu. Chipulumutso ndi chokwanira ndipo Yesu amapulumutsa kwathunthu (Ahebri 7:25). Palitu mpumulo waukulu pamene munthu adziwa kuti chipulumutso sitichipeza chifukwa cha ubwino wathu koma chifukwa cha chisomo ndi chifundo cha Mulungu. Malemba amenewa, kawirikawiri amagwiritsidwa ntchito pofuna kuphunzitsa za chitetezo chamuyaya, samachita zimenezo, ngakhale kuti ntchito zabwino ndizo chipatso cha chikhulupiriro chenicheni, chipulumutso chili chochokera ku chisomo basi ndipo sichochokera ku ntchito zathu. Mkhristu akuyenera kukhala odzipereka ku mphamu ya ntchito yoombola ya Khristu. Okhulupirira AKHOZA kukhala oteteze ka podziwa kuti chisomo cha Mulungu chimene chimabwezeretsa maubale owonongeka chidzakhala chokwanira kuwathandiza iwo kuti awusunge ubalewo."

## Zotsatira za chisankho

Pa Yohane 6:37-40 akunena kuti aliyense amene wabwera kwa Yesu sadzatayidwa kunja ndipo onse okhulupirira adzakhala ndi moyo wosatha. Ndimeyi siikunena za kuposa kwa chikhulupiriro koma za mphatso ya moyo wosatha kwa onse amene amukhulupirira Iye. Pambuyo pake, mu mutu womewu, timawerenga zakuti ambiri mwa ophunzira a Khristu anabwerera ndipo sanayendenso naye. Nthawi zonse anthu amakhala ndi chisankho chakuchoka pamaso pa Mulungu, kumene kuli ngati kuchoka ku chipulumutso chawo chomwe. Komanso pa Yohane 10:27-29 akunena za Yesu kuti akupereka moyo wosatha kwa nkosa zake "ndipo sizidzaonongeka

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

kunthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatala m'dzanja langa." Palibe munthu kapena mphamvu kupatula ife eniake amene tili ndi kuthekera kwakulanda mphatso cha chipulumutso imene Mulungu wayikiza mwa ife, amene tili nkhosa zimene Yesu anazinena kuti ndi zimene zimamva mau ake ndi kumutsatira (v 27). Ngati nkhosazo mwa kufuna kwao zisiya kutsata Yesu,

izo zichoka mwadala ndipo zimakhala kunja kwa chitetezo chimene chili m'dzanja la Atate.

Palitu mpumulo waukulu pamene mudziwa kuti palibe chimene chingathe kutilekanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu (Aroma 8:35-39). Chisankho chathu ndicho chinthu chokhacho chimene chimadula ubale wa chikhulupiro ndi chikondi pamene izi zabwezeretsedwa. Zotsatira za kusankha kwathu zilipo ngakhale lero kwa anthu onse "Malipiro amene uchimo umalipira ndi imfa. Koma mphatso yauleri imene Mulungu amapereka ndi moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye athu." (Aroma 6:23).

**"Pamene okhulupirira  
asiya kukhala mwa  
Yesu, ubale wawo  
umadulidwa ndipo  
zotsatira zake ndi  
chilango chosatha  
osati moyo wosatha."**

lapansi, koma pokhapo pamene iwo asunga chikhulupiro chawo potsata Khristu. Yesu anatambasula za mpesa ndi nthambi zake mu Yohane 15:1-11. Ngati nthambi sikubala chipatso, idulidwa ndi kutayidwa. Ife tikulangizidwa kuti "tikhalebe" mwa Khristu. Ngati sitikhala kapena kukhazikika mwa Khristu, tidzatayidwa ndi kuotchedwa. Chipatso ndi chilungamo chonse chimachokera mu kukhala mwa Khristu, popeza popanda Iyeyo ife tili chabe. Pamene okhulupirira asiya kukhala mwa Yesu, ubale wawo umadulidwa ndipo zotsatira zake ndi chilango chosatha osati moyo wosatha.

Baibulo limanena mwachimvekere kuti osalungama sakalowa mu Ufumu wa Mulungu (1 Akorinto 6:9-11). Ngati wina wavomereza chikhulupiro chake mwa Khristu ndipo wapulumutsidwa, koma kenaka nkutembenuka kupita ku ntchito zathupi, iyeyo watayika ku uzimu. Ahebri 12:14 amatiphunzitsa kuti popanda chiyero sittingathe kuona Mulungu. Chiyero chenicheni chimabwera kuchokera kwa Yesu, koma ngati timusiya Yesu, sitidzakhala oyera, ndipo ngati sitili oyera, sitidzaona Atate. Ndime 15 akunena kuti, "ndi kuyang'anira kuti

pangakhale wina wakuperewera chisomo cha Mulungu, kuti ungapuke muzu wina wa kuwawa mtima ungavute inu, ndipo aunyinji angadetsedwe nao" zoonadi, okhulupirira akuyenera kuvomereza ntchito ya Mulungu yochitika mwa chisomo apo ayi zotsatira zake ndi kulephera ndi kudetsedwa. Zimenezi zimatsutsana ndi chiphunzitso cha chitetezo chamuyaya.

### **Machenjezo akuti tisabwerere m'mbuyo**

Pali malemba ochuluka mu Chipangano Chatsopano amene amatichenjeza za kubwerera m'mbuyo ndipo amapereka umboni wakuti chipulumutso chikhaza kutayika ndipo chikhulupiro chikhaza kuonongeka. Mu fanizo la wofesa mbeu pa Mateyu 13:3-9 akutionetsa zoona zake za anthu amene anapulumuka koma kwakanthawi pamene mayesero abwera, iwo amafota popeza sanalole mau a Mulungu kuti azike mizu. Pa 1 Timoteo 4:1 amatichenjeza kuti ena "adzataya chikhulupiro chao," ndipo pa Agalatiya 5:1 akutichenjeza kuti "Muzichilimikira tsono, osalola kumangidwanso m'goli la ukapolo." Ayuda amene anabwerera m'mbuyo kuitanso ku lamulo koma atalandira kale chipulumutso "adalekana ndi madalitso aulere a Mulungu" (v4). Pa 1 Timoteo 6:9-11 akunena za iwo amene "adasiya njira ya chikhulupiro." Oyera mtima akulangizidwa pa Ahebri 3:12-14 kuti asamale kuopa kuti akhoza kusiya Mulungu ndi mtima woipa wa kusakhulupirira. Ngati wokhulupirira, pokhala Nyumba ya Mulungu ya Mzimu Woyer, adetsa nyumbayo imene poyamba inali yoyer, Mulungu adzaononga nyumbayo (1 Akorinto 3:16-17). Mulungu anapereka kwa mipingo ya ku Chivumbulutso mwai wakuti ikhoza kulapa chifukwa yambiri mwa iyo inali itatayika ndipo inadetsa zovala zavo.

Pa 2 Petro 2:20-22 akunena mosazungulira za iwo amene anapulumutsidwa koma anakodwanso ndipo akunena zakuti chitsiriziro chawo chidzakhala choipa koposa poyamba chifukwa chakuti anachoka pa choona.

### **Musasunthike**

Pali umboni wochuluka wochezeka m'malemba wotsimikiza kuti pamene anthu apulumuka, amakhalabe ndi mphamvu yosiya chikhulupiro chawo choyamba mwa Khristu nasiya njira yawo ya chipulumutso. Ndi chifukwa cha ichi, atumwi aja adanena mobwerezabwereza kuti "Koma tsono muzikhala okhazikika kolimba pa maziko a chikhulupiro chanu, osasunthika pa chiyembekezo" (Akolose 1:21-23), "limbikani, khalani osagwedezeza" (1 Akorinto 15:58), ndipo "Uzimenya nkhondo yabwino ya kusunga chikhulupiro, mpaka ukalandire moyo wosatha" (1 Timoteo 6:12).

Chiphunzitso cha chitetezo chamuyaya ndi chotsutsana ndi choonadi cha mau a Mulungu. Mphamvu ya Mulungu ndi yokwanira kutisunga ife kuti tisachimwe ndi kutithandiza kuti tikhale m'moyo wachiyo mwa chisomo chake. Tiyen'i tikhale maso, osadalira ntchito zathu koma mwachikhulupiro kudalira mwazi wa Yesu pamene tikutumikira Mulungu mwachiyero. Iye akhoza ndipo adzatisunga ndi kutiteteza ife kuchokera ku choipa chilichonse pamene tilola chiyero chake kuti chigwire ntchito m'miyoyo yathu. ■



# Funso Yankho ?

**Malingana ndi Ahebri 6:4-6 komanso  
Ahebri 10:26-29, kodi nkosatheka  
kwa munthu amene wapulumuka  
kenaka nkuchoka ku chikhulupiriro  
nayamba moyo wauchimo kuti  
abwezeretsedwenso ku chipulumutso?**

Tikunena motsimikiza kuti AYI! Ndi zotheka ndithu kuti munthu amene anabwerera m'mbuvo apulumutsidwe. Maziko a uthenga wabwino ndiwo akuti chikondi cha Mulungu ndi chachikulu kwa anthu ndipo pali chiyembekezo cha kubwezeretsedwanso kudzera mu mwazi wa Yesu Khristu. Pa 2 Petro 3:9 akutiuza kuti Mulungu "Safuna kuti ena aonongedwe, koma afuna kuti onse atembenuke mtima." Ambuye safuna kuti aliyense ataye moyo wake kwamuyaya; ndipo chifukwa cha ichi, iye amagwira ntchito kudzera mu mphamvu ya kutsutsa uchimo imene ili mwa Mzimu wake Woyeru pofuna kuitanira anthu onse kwa iye Mwini. Muitano umene uli pa Chivumbulutso 22:17, wakuti "Aliyense wowafuna, awalandire mwaulere madzi opatsa moyo," ukupitanso ngakhale kwa iye amene wabwerera m'mbuvo. Mu Chipangano Chakale amanena mobwerezabwerezza za chikhaldwe cha Mulungu chokhululuka ndi kufuna kuyanjananso ndi mtundu wa Israele umene unamuchimwira. Ngakhale kuti pali chisomo chakukhala m'moyo wachikhristu wachigonjetso, ngati wina wataya chipulumutso chake chifukwa cha uchimo, sizitanthauza kuti palibenso chiyembekezo makamaka ngati pali mtima wofuna kulapa ndi kumvera Mulungu. Kubwezeretsedwanso ndi chinthu chimene chikuperekedwa kwa anthu ONSE.

Tatiyeni tiganizire za tanthauzo la Ahebri 6:4-6 ndi Ahebri 10:26-29 pamene tikulingalira za choonadi chili m'mwambamu. Ndime ziwiri izi za ku Ahebri zikufanana mu tanthauzo ndi kumasulira. Pa Ahebri 6:4-6 akunena kuti: "Pakuti sikutheka kuwakonzanso, atembenuke mtima, iwo amene anaunikidwa pa nthawi yake, nalawa mphatso ya Kumwamba, nakhala olandirana naye Mzimu Woyeru, nalawa mau okoma a Mulungu, ndi mphamvu ya nthawi ilinkudza, koma anagwa m'chisokero; popeza adzipachikiranso okha Mwana wa Mulungu, namchititsa manyazi poyeru." Tikangowawonera chapamwamba mauwa,

tikhoza kuona ngati chipulumutso ndi chosatheka kwa anthu amene kanthawi kena analawa mphamvu ya chisomo cha Mulungu cha kupulumutsa. Tikuthokoza kuti pamene tiphunzira malemba timazindikira kuti pali choonadi china. Zindikirani kuti chifukwa chimene chikuperekedwa chakuti ndi kosatheka "kuwafiksanso pa kulapa"ndicho chakuti iwovo akumupachikanso Khristu. Kodi anthu adzapulumuka bwanji ngati akana mphamvu ya mwazi wa Yesu? Pamene wina wake akana mphamvu ya Yesu yakupulumutsa ku machimo, nkosatheka kuwafiksanso ku



kulapa. Ngati wina asiya kupachika Khristu kachiwirinso m'moyo uno navomereza mphamvu ya mwazi, akhoza kubwezeretsedwanso ndipo samuchititsanso Khristu manyazi. Malemba sakunena za iwo obwerera m'mbuvo koma za anthu amene asiya chikhulupiriro nakana nsembe yopepesera machimo ya Khristu mwini wake.

Chimodzimodzinso, pa Ahebri 10:26 akunena kuti: "Pakuti tikamachimwirachimwira mwadala, kwina tikudziwa choona, palibenso nsembe ina iliyonse ingaperekedwa chifukwa cha machimo athuwo." Lemba ili palokha likufuna kunena kuti palibenso, koma ma vesi awa akulongsola tanthauzo lake la nsembe ya uchimo kwa iye wobwerera m'mbuvo. "Pakuti tikachimwa ife eni ake, titatha kulandira chidziwitso cha choonadi, siitsalanso nsembe ya kwa machimo, koma kulindira kwina koopsa kwa chiweruziro, ndi kutentha kwake kwa moto wakuononga otsutsana nao. Munthu woepesuta chilamulo cha Mose angofa opanda chifundo pa mboni ziwiri kapena zitatu: ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa chipangano umene anayeretsedwa nao chinthu wamba, nachitira chipongwe Mzimu wa chisomo" (Ahebri 10:27-29). Ndime izi zikufotokoza momveka bwino za mutu umenewu.

Palibenso nsembe ina ya uchimo koposa mwazi wa Yesu Khristu. Ngati nsembe yokezeke. Padzakhala chilango chokhwima kwa iwo amene apulumutsidwa koma kenaka ndi kukana mwazi wa chipangano. Malemba tikuwanenawa sakuphunzitsa kuti wobwerera m'mbuyoyo sangathe kubwezeretsedwa ku chipulumutso, koma iwo amaphunzitsa kuti chipulumutso ndi chosatheka kwa iye amene wabwerera ngati iye apitirira kuukana mwazi wa Yesu ngati njira yoladirira chipulumutso. "Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." (Machitidwe 4:12). Pamene munthu wosakhulupirira wobwerera m'mbuvo uja asintha mtima wake ndi maganizo ake navomereza nsembe ya mwazi, Mulungu adzamupulumutsa ndi chifundo komanso chisomo chake. ■



KODI MUKUDZIWA?

77 mwa anthu 100 aliwonse ku America amakhulupirira kuti chipulumutso cha munthu chimabwera chifukwa chochita ntchito zabwino.

52 mwa anthu 100 akiwonse amanena kuti ntchito zabwino zikhoza kumupangitsa munthu kuti akalowe kumwamba.

60 mwa anthu 100 aliwonse amakhulupirira imfa ya pamtanda ya Yesu Khristu ndiyo nsembe yokhayo imene ikhoza kuchotsa chilango cha uchimo.

*The State of American Theology, LifeWay Research, 2016*

65 mwa anthu 100 akhristu aliwonse amakhulupirira kuti pali njira zingapo zopitira kumwamba.

*U.S. Religious Landscape Study, Pew Research Center, 2014*



## MKAZI WA MTUMIKI

*Onani, mdzakazi wanu ali kapolo wakusambitsa mapazi a anyamata a mbuye wanga. —1 Samuele 25:41b*

### Kuti Mutipeze

The Gospel Truth  
P. O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)

### CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Akazi a atumiki nawonso ndi anthu ndipo amakhala ndi zosowa zavo monga alili munthu wina aliyense. Nthawi zambiri amakhala okhaokha ndipo amadziona kuperewera kuti atumikire, namaganiza kuti mwina ali ngati munthu wakuti wabisala pachipande pamene aliyense akuwaona ndipo sangathe kuchita zinthu zofuna zavo. Amakhala wokakamizika kuti afikire ndi kukwaniritsa ku zofuna zochuluka za pa mpingo.

Mkazi weniweni wa mtumiki ndi wolimbikira ntchito amene ntchito zake zimadutsa za mai kapena mkazi wa munthu wina wadera. Iye amaphikira odwala, amaphunzitsa ana, amatsekula nyumba yake kwa alendo, amakonza chakudya chakuti gulu la anthu lidye lamulungu madzulo, amalangiza ndiponiso kupemphera ndi anthu amene ali osowa, amayankha ma foni ndi ma uthenga obwera pa foni (ma sms), amakonza ndi kukongoletsa mu tchalichi, ndipo amaima m'malo mwa mwamuna wake komanso amachita zina zambiri.

Ntchito imodzi yaikulu ndi yovuta imene amaigwira ndiyo yokhala mnzake, wosungirana naye chinsinsi ndipo munthu wodalirapo wa mwamuna wake. Iye amamva mavuto ndi zobetchera za mtumiki amene ali mwamuna wake. Iye amaona chamaso zosautsa zimene anthu amamuchitira mwamuna wakeyo. Iye amalingalira zonse zimene mwamuna wake amayesetsa kuchita komabe nkumamva anthu akumunena. Ndipo iye amapeza chikhululukiro mwa Khristu namapitirabe kuwakonda ndi kuwatumikira anthu omweomwewo amene amakhalabe osayamika.

Akazi a atumiki okwana 80 mwa 100 aliwonse amanena kuti sayamikiridwa ndi mamembala a mpingo wao. Choncho, kwa iwo amene ali akazi a atumiki, ife tikuti zikomo chifukwa cha ntchito yaikulu imene mumaiigwira. Sitikuyembekeza kuti muchita zonse mwa myaa ngati angelo ndipo tikuzindikira kuti ndinu anthu ngati m'mene tilili ifeyo. Zikomo kwambiri chifukwa chopitirira kutumikira. Zikomo kwambiri chifukwa chotikonda ndi kutipempherera ngakhale timachita zinthu zimene zili zokusautsani. Zikomo kwambiri chifukwa choima naye mwamuna wanu amene ali mtumiki wathu. Zikomo kwambiri chifukwa cha chikondi ndi kutumikira kwanu zimene zili zaumulungu. Timakukondani ndi kukunyadirani!